



# Ubwino ndi Malamulo a Adhana (Shafi'i)



Kabukuka kakonzedwa mogwirizana ndi Fiqh ya Shafi'i, zosintha, kukonza komanso zowonjezera kuchokera n'kabuku ka "Faizan-e-Azaan" kolembedwa ndi Shaykh-e-Tariqat, Ameer-e-Ahle Sunnat, muyambitsi wa Dawat-e-Islami, Hazrat Allama Maulana Abu Bilal Muhammad Ilyas Attar Qadri Razavi (madalitso ake apamwamba apitirire).

laperekedwa ndi:  
Al-Madina-tul-Ilmiyyah  
Islamic Research Center

آذان کے فضائل و مسائل (شافعی)  
Azaan kay Fazaail-o-Masa'il (Shaafi'i)

# Ubwino komanso Malamulo apa Azaan (Shafi'i)

**Kabukuka** kaperekedwa mu Chiurdu ndi Majlis Al-Madina-tul-'Ilmiyyah. **Nthambi Yomasulira (Dawat-e-Islami)** yamasulira mchichewa. Ngati mungapeze cholakwika chilichonse pakulemba kapena kumasulira, chonde dziwitsani Nthambi Yomasulirayi pa imelo kapena keyala iyi ndi cholinga cholandira mphotho [Sawab].

## Nthambi Yomasulira (Dawat-e-Islami)

Aalami Madani Markaz, Faizan-e-Madinah, Mahallah Saudagran,  
Purani Sabzi Mandi, Karachi, Pakistan

UAN: ☎ +92-21-111-25-26-92 - Ext. 7213

Imelo: 📧 [translation@dawateislami.net](mailto:translation@dawateislami.net)

**Ubwino komanso Malamulo apa Azaan (Shafa' i)**  
Kumasulira m'Chichewa kwa Buku lotchedwa 'Azaan kay Fazaail-o-  
Masa'il (Shaafi'i)'

**Mawumwini onse ndi otetezedwa**

© 2025 Maktaba-tul-Madinah

Palibe gawo lililonse la bukhuli lomwe lingasindikizidwenso, kapena kufalitsidwa mwanjira ina iliyonse ngati, pakompyuta, pamakina, kujambula kapena mwanjira ina, popanda chilolezo cholembedwa ndi Maktaba-tul-Madinah.

**Kusindikizidwa koyamba :** Rabi'-ul-Awwal, 1447 AH - (Aug, 2025)

**Lamasuliridwa ndi:** Nthambi Yomasulira (Dawat-e-Islami)

**Wosindikiza:** Maktaba-tul-Madinah

**Kuchuluka:** -

### Thandizo

Chonde khalani omasuka kulankhulana nafe ngati mukufuna kuthandizira kusindikiza buku lachipembedzo kapena kabuku kuti likhale Isal-e-Sawab ya achibale anu omwe anamwalira.

#### **Maktaba-tul-Madinah**

Aalami Madani Markaz, Faizan-e-Madinah Mahallah Saudagran,  
Purani Sabzi Mandi, Bab-ul-Madinah, Karachi, Pakistan

✉ **Imelo:** maktabaglobal@dawateislami.net

maktaba@dawateislami.net

☎ **Foni:** + 92-21-34921389-93

💻 **Webusaiti:** [www.dawateislami.net](http://www.dawateislami.net)

الْحَمْدُ لِلَّهِ رَبِّ الْعَالَمِينَ وَالصَّلَاةُ وَالسَّلَامُ عَلَى خَاتَمِ النَّبِيِّينَ  
أَمَّا بَعْدُ فَأَعُوذُ بِاللَّهِ مِنَ الشَّيْطَانِ الرَّجِيمِ بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَنِ الرَّحِيمِ

## Du'a yowerengera bukuli

**W**erengani Du'a yosatirayi (Pempho) musanayambe kuwerenga buku lililonse la chipembezo kapena buku la chisilamu, muzakumbukira chilichonse chomwe muzawerenga, **إِنْ شَاءَ اللَّهُ**:

اللَّهُمَّ افْتَحْ عَلَيْنَا حِكْمَتَكَ وَانْشُرْ  
عَلَيْنَا رَحْمَتَكَ يَا ذَا الْجَلَالِ وَالْإِكْرَامِ

### Janthawuzo

O Allah عَزَّوَجَلَّ Titsekulireni khomo la nzeru komanso la kuzindikira ndipo mutichitire chifundo, O! inu yemwe ndi wolemekezeka komanso Wawulemerero.

(Al-Mustatraf, vol. 1, pp. 40)

**Dziwani:** mfunireni zabwino (Salat-‘Alan-Nabi ﷺ) kamodzi kumayambiriro komanso kumapeto kwa Du'a.

## zankatimu

|                                                              |    |
|--------------------------------------------------------------|----|
| Poyamba werengani izi .....                                  | 1  |
| Ubwino ndi Malamulo apa Azaan (Shafi ' i) .....              | 1  |
| Ubwino Wonfunira zabwino Mtumiki:.....                       | 1  |
| Mtumiki (ﷺ) anachita Azaan kamodzi .....                     | 2  |
| Ndi aazaan kapena azaan? .....                               | 2  |
| Hadith zisanu ndi zinayi zodala zokhuza ubwino wa azaan..... | 2  |
| 1 Palibe Tizilombo m'Manda .....                             | 2  |
| 2. Nyumba za Ngale.....                                      | 3  |
| 3. Machimo akale akhululukidwa.....                          | 3  |
| 4. Satana akuthawa 36 mailosi.....                           | 3  |
| 5. Azaan ndi njira yoyankhidwira mapemphero .....            | 4  |
| 6. Kukhululuka kwa muazzin.....                              | 4  |
| 7. Kutetezedwa ku mazunzo pa tsiku la azaan .....            | 4  |
| 8. Chithandizo cha manjenje.....                             | 4  |
| 9. Njira yochotsera chisoni .....                            | 5  |
| Nsomba zimafunanso kukhululukidwa.....                       | 5  |
| Ubwino Woyankha Azaan.....                                   | 5  |
| Pezani Zochita Zabwino 34.6 miliyoni tsiku lililonse.....    | 6  |
| Woyankha Azaan Analowa Kumwamba.....                         | 8  |
| Njira Yoyankhira Azaan ndi Iqamat.....                       | 9  |
| 29 Madani ngale zanzeru za Azaan komanso Iqamat.....         | 10 |
| 12 ngale za Madani zoyankhira Azaan ndi Iqamat .....         | 18 |
| 10 Nthawi zokondedwa (Mustahab) za kuchita Azaan .....       | 20 |

|                                                             |    |
|-------------------------------------------------------------|----|
| Mfunireni zabwino Mtumiki Wodalitsika musanayambe kuchita   |    |
| Azaan .....                                                 | 21 |
| Kunong'ona kwa Satana.....                                  | 21 |
| Yankhani kunong'oneza kwa satana uku.....                   | 21 |
| Mafunso ndi mayankho okhuza kusalemekeza Azaan.....         | 25 |
| Zitsanzo zisanu ndi zitatu za ziganizo za Kufriyah zokhudza |    |
| Azaan .....                                                 | 26 |
| Azan.....                                                   | 27 |
| Iqamat.....                                                 | 29 |
| Uthenga wabwino wopembedzera .....                          | 30 |
| Iman Mujmal [Chikhulupiro Mwachidule] .....                 | 31 |
| Kalimah Tayyib (kutanthawuza mawu oyera).....               | 32 |
| Kalimah yachiwiri Shahadah (kutanthawuza kuchitira umboni)  | 32 |
| Kalimah Tamjeed (kutanthawuza ukulu).....                   | 33 |
| Chachisanu Kalimah Istighfar (kutanthawuza kufunafuna       |    |
| chikhululuko) .....                                         | 34 |
| Kalimah Yachisanu ndi chimodzi Radd Kufr (kutanthawuza      |    |
| kukana kusakhulupirira).....                                | 35 |
| Perekani kabukuka kwa wina mukawerenga nokha .....          | 36 |

## Poyamba werengani izi

اَلْحَمْدُ لِلّٰهِ Mabuku komanso timabuku tolembedwa ndi Shaykh-e-Tareeqat Ameer-e-Ahl-e-Sunnat, yemwe ndi Muyambitsi wa Dawat-e-Islami 'Allamah Maulana Abu Bilal Muhammad Ilyas Attar Qadiri Razavi دَامَتْ بَرَكَاتُهُمُ الْعَالِيَةُ ndi omwe asunga chuma ndipo ndi olemera mu chidziwitso ndi nzeru zokhudzana ndi zikhulupiriro ndi ntchito, makhalidwe abwino ndi kupambana, Shariah ndi tareeqah, chiyambi komanso mbiri yakale, sayansi ndi mankhwala, makhalidwe ndi machitidwe, zochitika za tsiku ndi tsiku ndi zina zambiri. Choncho, Kutub-e-Fiqh-e-Shaafi'i, imene ndi nthambi ya Al-Madina-tul-Ilmiyyah (Likulu Lofufuza za Chisilamu) tsopano ikukonza mabuku posintha mofunikira ndi kuwonjezera monga momwe malamulo a Shaafi'i zimayendera kuti otsatira za malamulo a Shaafi'i azithanso kupindula ndi zolembe za Ameer-e-Ahl-e-Sunnat/ngale za Madani zomwe zili zolemera m'chidziwitso ndi nzeru.

- ❖ Tsatanetsatane wa ntchito yomwe Kutub-e-Fiqh-e-Shaafi'i anachita m'kabukuka kali motere: Malamulo onse omwe atchulidwa m'kabukuka amene asinthidwa ndi omwe atengedwa m'mabuku ovomerezeka kuchokera mu ziphunzitsa za Imam Shaafi'i.
- ❖ Malo ena, malamulo awonjezedwanso ngati kwayenera kutero potengera ziphunziso zake.

- ❖ Zosintha zachitika mu kabukuka potengera mawu a Dawat-e-Islami komanso nfundo zosinthidwa za Islamic Research Center ndi nthambiyi, Kutub-e-Fiqh-e-Shaafi'i.
- ❖ Pambuyo pomaliza ntchito yomwe tatchulayi, kabukhu konse kakawunikidwa kuchokera ku Shar'i ndi Mufti Muhammad Rafeeq Sa ' di Shaaf i 'i صَدِّقُهُ الْعَالِي.

Ubwino wonse kakabukuka kamene kali nako mosakayikira chifukwa cha tawfeeq yomwe Allah Wamphanvu zonse anapereka komanso mothandizidwa ndi Mtumiki wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ, kukondedwa kwa awliyah odalitsika komanso chikondi cha Amer Ahl e Sunnat. Cholakwika chilichonse chimene chingapezeke m'menemu ndi chifukwa cha kunyalanyaza kwathu kosadziwa.

**Al-Madina Al-Ilmiyyah (Likulu Lofufuza za Chisilamu) Nthambi ya mabuku a 'Fiqh Shaafi'i'**

**11 Jumad al-Ukhraa 1442AH/ 24 Januware 2021**



الْحَمْدُ لِلَّهِ رَبِّ الْعَالَمِينَ وَالصَّلَاةُ وَالسَّلَامُ عَلَى خَاتَمِ النَّبِيِّينَ  
أَمَّا بَعْدُ فَأَعُوذُ بِاللَّهِ مِنَ الشَّيْطَانِ الرَّجِيمِ بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَنِ الرَّحِيمِ

# Ubwino komanso Malamulo apa Azaan (Shafa ' i)

(Pezani zabwino zokwana 34.6 miliyoni tsiku lililonse.)

Werengani kabukuka [masamba 35] kuyambira koyambirira mpaka kumapeto. Ndizotheka kwambiri kuti mutha kupeza zolakwa zanu zambiri.

## Ubwino Womfinira zabwino Mtumiki:

Wokondedwa Mtumiki صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ wanena kuti: “Yemwe wawerenga Qur'an yopatulika, namutamanda Allah Wamphanvu zonse, ndikuwerenga salat kwa Mtumiki (صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ) namupempha chikhululuko Mbuye wake, ndiye kuti wapeza ubwino kuchokera pa malo pake.”<sup>1</sup>

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

---

<sup>1</sup> Shu'ab al-Iman, juz. 2, p. 373, Hadith 2084

## Mtumiki (ﷺ) anachita Azaan kamodzi

Mtumiki wokondedwa ﷺ nthawi ina anachita azaan ali pa ulendo ndipo anayankhula mawu a Shahadah (kuyikira umboni) motere, أَشْهَدُ أَنْ رَسُولُ اللَّهِ (Ndikuyikira umboni kuti ineyo ndi Mtumiki wa Allah).”<sup>1</sup>

## Ndi aazaan kapena azaan?

Anthu ena amati 'aazaan', zomwe ndizolakwika. Aazaan ndi mawonekedwe ochulukitsa a 'uzn' ndipo 'uzn' amatanthawuza 'khutu'. Katchulidwe kolondola ndi azaan. Tanthawuzo lenileni la azaan ndi kuchenjeza.

# Ma Hadith asanu ndi anayi odala okhuza ubwino wa azaan

## 1 Palibe Tizilombo m'Manda

Mtumiki (Rasool) wokondedwa ndi wodalitsika wa Allah ﷺ anati, ‘Amene amapereka Adhana (Mpempho loyitanira ku Swala) pofuna kupeza Sawab (malipiro abwino), ali ngati Shahidi (wophedwera chikhulupiriro) woviyikidwa m'mwazi. Ndipo akamwalira, tizilombo sitidzadya thupi lake

---

<sup>1</sup> Tuhfah al-Muhtaj, juz. 1, p. 262; Fatawa Razawiyyah, juz. 5, p. 375

Ubwino komanso Malamulo apa Azaan (Shafa' i)

m'manda (ndiko kuti, thupi lake lidzakhala lotetezedwa ku tizilombo).<sup>1</sup>

## 2. Nyumba za Ngale

Ndinapita ku Paradayiso kumene ndinawona nyumba za ngale; fumbi lawo linali la misk. Ndinamufunsa kuti, 'E iwe Jibrail! Kodi nyumbazi ndi za ndani?' Anayankha modzichepetsa kuti: 'Kwa ma imamu ndi ma Muazzin a Ummah wanu.'<sup>2</sup>

## 3. Machimo akale akhululukidwa

Amene akuyitanira azaan Swala zisanu pa tsiku chifukwa cha chikhulupiriro ndi cholinga chopeza malipiro, adzakhululukidwa machimo ake am'mbuyomu, ndipo adzakhululukidwa machimo am'mbuyomu a amene akuwatsogolera anzake mu Swala zisanu za tsiku chifukwa cha chikhulupiriro kuti alandire malipiro.<sup>3</sup>

## 4. Satana amathawa 36 mayilos

Satana akamanvera azaan pa swalah, amathamanga nakafika ku Rauha. Wolemba nkhanu wanena kuti Rauha ili pantunda

---

<sup>1</sup> Gwero: Mu'jam-ul-Kabeer, ts. 312, vol. 12, Hadith 13516

<sup>2</sup> Jami' Saghir, p. 255, Hadith 4179

<sup>3</sup> Kanz-ul-Ummal, juz 7, p. 279, Hadith 20902

Ubwino komanso Malamulo apa Azaan (Shafa' i)  
wa makilomita 36 kuchokera ku Madinah Munawwarah.<sup>1</sup>

## 5. Azaan komanso njira yoyankhidwira mapemphero

Pamene woyitana azaan akuyitana, zitseko zakumwamba zimatsegulidwa, ndipo pempherolo limayankhidwa.<sup>2</sup>

## 6. Kukhululuka kwa muezzin

Muezzini amakhululukidwa pamalo pomwe mawu ake afika, ndipo chilichonse cha pantunda ndi m'madzi chonva mawu ake chimampempha chikhululukiro.<sup>3</sup>

## 7. Kutetezedwa ku mazunzo pa tsiku la azaan

Malo amene azaan amapangidwira atetezedwa tsiku limenelo ndi Allah Wamphanvu zonse ku chilango Chake.<sup>4</sup>

## 8. Chithandizo cha manjenje

Pamene Adam عَلَيْهِ السَّلَام anatsikira ku India kuchokera ku Paradiso anachita mantha, choncho Jibrail عَلَيْهِ السَّلَام anatsika namuchitira Azaan.<sup>5</sup>

---

<sup>1</sup> Muslim, p. 151, Hadith 388

<sup>2</sup> Mustadrak, juz. 2, p. 243, Hadith 2048

<sup>3</sup> Musnad Imam Ahmad, juz. 3, p. 453, Hadith 6346

<sup>4</sup> Mu'jam Kabeer, juz. 1, p. 199, Hadith 745

<sup>5</sup> Hilyah al-Awliya', juz. 5, p. 123, Raqam 6566

Ubwino komanso Malamulo apa Azaan (Shafa' i)

## 9. Njira yochotsera nkhawa

O Ali! Ndimakuphezani wokhumudwa; wuzani aliyense wa m'banja mwanu kuti akuchitireni azaan m'makutu mwanu chifukwa amachotsa kukhumudwa ndi nkhawa.<sup>1</sup> Pambuyo pofotokoza nkhani imeneyi, Imam Ahmad Raza Khan anatchula pa pg. 668 ya Fatawa-e-Razawiyyah, vol. 5. Sayyiduna Ali ndi chiwerengero cha olemba nkhani kwa iye onse anati: “فَجَرَّيْتُهُ فَوَجَدْتُهُ كَذَّالِكَ” (Pamene tinayiyesa, tinapeza chimodzimidzi).<sup>2</sup>

## Nsomba zimafunanso kukhululukidwa

Kwanenedwa kuti, “Chilichonse, kuphatikizapo nsomba za m'nyanja, zimapempherera chikhululukiwo kwa amene akufuwula pochita azaan. Muazin akayitana Azaan, angelo nawonso amabwereza, ndipo akamaliza [azaan], angero amamupempherera chikhululukidwa mpaka tsiku lachiweruzo. Amene wamwalira ngati muazini sadzalangidwa m'manda ake ndipo amakhala wotetezeka ku zowawa panthawi ya infa. Komanso amakhala otetezeka ku chilango ndi kufinyika kwa mmanda.”<sup>3</sup>

## Ubwino Woyankha Azaan

Wokondedwa Mtumiki صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ nthawi ina amati: “E

---

<sup>1</sup> Jami' al-ahadith, juz. 15, p. 339, Hadith 6017

<sup>2</sup> Mirqat al Mafatih, juz. 2, p. 310; Jami' Al-ahadith, juz. 15, p. 339, Hadith 6017

<sup>3</sup> Tafseer Surah Yousuf, Imam al-Ghazali, p. 14

Ubwino komanso Malamulo apa Azaan (Shafa' i)

inu akazi! Nthawi zonse mukanva Bilal akuyitana azaan ndi iqamat, inunso muzinena zomwe akunena, chifukwa pa kalimah iliyonse, Allah Wamphanvu zonse adzakulemberani zabwino zikwi zana limodzi, ndikukukwezani nyota zanu chikwi chimodzi ndikukukhululukirani chikwi chimodzi cha machimo anu.” Akaziwo atanva izi anafunsa kuti, “Izi ndi za akazi; kwa amuna nchani?” Mneneri wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ anayankha: "Amuna azapeza chimodzimodzi kawiri." <sup>1</sup>

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

### Pezani Zochita Zabwino 34.6 miliyoni tsiku lililonse

E, okonda Swalah! Ndi chifundo chachikulu chotani cha Mulungu Wamphanvu zonse! Watifewetsa kwambiri kuti tipeze ntchito zabwino, tikweze manyota athu ndi kutikhululukira machimo athu, koma zachisoni, ndife osalabadira ngakhale kuti ndife opepuka komanso osavuta. Tsatanetsatane wa ubwino woyankha azaan komanso iqamat zomwe zatchulidwa mu Hadith yodalitsika yomwe tatchulazi ndi motere.

اللَّهُ أَكْبَرُ اللَّهُ أَكْبَرُ ndi ma kalimaat awiri. Mwanjira iyi, azaan yonse imakhala ndi ma kalimaat 19 kuphatikiza tarje'e. Mlongo wachisilamu akayankha azaan imodzi, mwachitsanzo kunena

---

<sup>1</sup> Tarikh Ibn Asakir, Raqm 6892; Muhammad Bin Umar, juz. 55, p. 75

Ubwino komanso Malamulo apa Azaan (Shafa' i)

zomwe muazin akunena, adzapeza zabwino 1.9 miliyoni, nyota zake zidzakwezedwa ndi 19,000 ndipo 19 sawuzande amachimo ake adzakhululukidwa. Pali malipiro owirikiza kawiri kwa abale achisilamu.

Pali ma azaan awiri a Fajr, ndipo iwo muli **اَلصَّلٰوةُ خَيْرٌ مِّنَ النَّوْمِ** kawiri pa chilichonse. Mwanjira imeneyi, pali kalimaat 21 kuphatikiza tarje'e mu Fajr azaan imodzi, ndipo mu azaan onse muli ma kalimaat 42. Momwemonso, poyankha onse awiri azaan a Fajr, mlongo wachisilamu adzalandira zabwino 4.2 miliyoni, nyota zake zidzakwezedwa ndi 42,000 [zikwi makumi anayi ndi ziwiri] komanso 42,000 [zikwi makumi anayi ndi ziwiri] za machimo ake zidzakhululukidwa. malipiro onsewa adzakhala kawiri kwa abale achisilamu. Pali makalimaat 11 mu iqamat, kotero poyankha iqamat, mlongo wachisilamu atha kupeza zabwino 1.1 miliyoni [1 miliyoni 1 handiredi sowuzande], nyota zake zidzakwezedwa ndi 11,000 [11,000] ndipo machimo 11,000 [11,000] adzakhululukidwa. Mwachidule, ngati mlongo wachisilamu atakwanitsa kuyankha azaan komanso iqamat ya salah zisanu za tsiku ndi tsiku, adzapeza zabwino 17.3 miliyoni [17.3 miliyoni ] tsiku lililonse, nyota zake zidzakwezedwa ndi 173,000 [zana ndi makumi asanu ndi awiri. -zikwi zitatu], ndipo machimo ake 173,000 [173,000] adzakhululukidwa, ndipo malipiro ake adzakhala owirikiza kwa Asilamu. abale. M'mawu ena, m'bale wachisilamu adzapeza zabwino 34.6 miliyoni [mamiliyoni makumi atatu ndi anayi ndi mazana asanu ndi limodzi ndi mazana asanu ndi limodzi], nyota zake

Ubwino komanso Malamulo apa Azaan (Shafa' i)

zidzakwezedwa ndi 346,000 [sauzande mazana atatu mphambu makumi anayi kudza zisanu ndi chimodzi] ndi machimo 346,000 [sauzande mazana atatu makumi anayi ndi zisanu ndi chimodzi. ] adzakhululukidwa.

## Woyankha Azaan Analowa Kumwamba

Sayyiduna Abu Hurayrah رَضِيَ اللهُ عَنْهُ wanena kuti: [Nthawi ina] anamwalira munthu yemwe sanali kudziwika ntchito zake yayikulu ankagwira. Pamaso pa maswahaaba odalitsidwa (popereka nkhani zobisika), Mtumiki wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ anati: “Inu mukudziwa kuti Mulungu anampatsa Paradiso. Anthuwo anadabwa, popeza kuti analibe ntchito [yabwino] iriyonse. Choncho mmodzi mwa maswahaaba anapita kunyumba kwa munthuyo namufunsa nkazi wake wamasiye (رَضِيَ اللهُ عَنْهَا) Kodi ntchito yake yapaderayi inali chani? Iye anayankha kuti: “Sindikudziwa chilichonse mwa ntchito zake yapaderayi, koma ndikudziwa chinthu imodzi kuti kaya usana kapena usiku, akamanva azaan, amayankha ndithu.<sup>1</sup> Allah Wamphanvu zonse amuchitire chifundo ndi kutikhululukira chifukwa cha iye.

آمِينَ بِجَاهِ النَّبِيِّ الْأَمِينِ صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ

*Gunah-e-Gada ka Hisab Kiya woh Agar cheh Lakh akuti hayn Siwa*

*Magar Aye 'Afu Tayray 'Afu ka tou Hisab Hay nah Shumar hay*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

---

<sup>1</sup> Tarikh Ibn Asakir, Raqm 4707, Ata` bin Qara, juz. 40, pp. 412-413



## Njira Yoyankhira Azaan ndi Iqamat

Muezzin atchule kalimaat ya azaan ndi kuyima. Kunena ma takbir awiri mu mpweya umodzi uku akuchita azaan ndi Sunnah. Kupatula izo, makalima'at onse otsalawo adzanenedwa mosiyana.<sup>2, H</sup> Muazin akayamba azaan, amene akunvetsera awerenge motere: **مَرْحَبًا بِالنَّاقِلِ عَدَا، مَرْحَبًا بِالصَّلَاةِ أَهْلَا** (Takulandirani kwa amene wanena chilungamo).<sup>1</sup> Muazin akamaliza **أَللَّهُ أَكْبَرُ اللَّهُ أَكْبَرُ**, anenenso kuti **أَللَّهُ أَكْبَرُ اللَّهُ أَكْبَرُ**. Muazin akanena kuti **أَشْهَدُ أَنْ لَا إِلَهَ إِلَّا اللَّهُ**, nayenso abwerezenso **صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ**. Woyankha akanva dzina la Muhammad mu azaan adzanene kuti **مَرْحَبًا بِحَبِيبِي وَفُتَاتَةِ عَيْنِي مُحَمَّدَ بْنَ عَبْدِ اللَّهِ**, ndikupsompsona zala zake zazikulu ndi kuziyika m'maso mwake.<sup>3</sup> Muazin akamaliza kunena kuti **أَشْهَدُ أَنَّ مُحَمَّدًا رَسُولَ اللَّهِ**, nayenso abwerezenso **سَمِعَ عَلَى الْفَلَاحِ**, woyankhayo ayankhe motere: **سَمِعَ عَلَى الْفَلَاحِ، عَلَى الصَّلَاةِ ط وَلَا حَوْلَ وَلَا قُوَّةَ إِلَّا بِاللَّهِ**, ndipo Muazin akanena **سَمِعَ عَلَى الْفَلَاحِ، اللَّهُمَّ اجْعَلْنَا مُفْلِحِينَ، لَا حَوْلَ وَلَا قُوَّةَ إِلَّا بِاللَّهِ**, Woyankha anene kuti **أَشْهَدُ أَنَّ مُحَمَّدًا رَسُولَ اللَّهِ**, woyankhayo abwerezenso **أَشْهَدُ أَنَّ مُحَمَّدًا رَسُولَ اللَّهِ**, Munthawi ya Fajr azaan poyankha **الصَّلَاةُ خَيْرٌ مِنَ النَّوْمِ**, woyankha anene: **صَدَقَتْ وَبَرَزَتْ وَبِالْحَقِّ نَطَقَتْ**.<sup>5</sup>

---

<sup>1</sup> *Ia'nat al-Talibeen*, juz. 1, p. 413

<sup>2</sup> *Tohfa al Muhtaj*, juz. 1, p. 215

<sup>3</sup> *Ia'nat al-Talibeen*, juz. 1, p. 413

<sup>4</sup> *Tohfa al Muhtaj*, juz. 1, p. 215

<sup>5</sup> *Tohfa al Muhtaj m'a Hashiyah Sharwani*, juz. 2, p. 112

Mnthawi yanvula yankuntho, mdima wandiweyani ndi mphepo yamkuntho, zili Sunnah kwa muazin kunena ‘أَلَا صَلُّوا فِي رِحَالِكُمْ’ [kawiri] pambuyo pa ‘حَيَّ عَلَى الْفَلَاحِ’ uku akuyitanira azaan bwino kwambiri ngati atanena izi. Amene akunvera ayankhe لَا حَوْلَ وَلَا قُوَّةَ إِلَّا بِاللَّهِ.<sup>1</sup>

Ndi Sunnahnsa kuyankha iqamat. Ikhozanso kuyankhidwa mofananamo. Kusiya kokha ndiko kuti poyankha قَدْ قَامَتِ الصَّلَاةُ woyankhayo anene kuti أَقَامَهَا اللَّهُ وَأَدَمَهَا مَا دَامَتِ السُّبُوتُ وَالْأَرْضُ وَجَعَلَنِي مِنْ صَالِحِ أَهْلِهَا (Tanthawuzo lake: Mulungu Wamphanvu zonse alikhazikike mpaka thambo ndi nthaka zikhalepo ndipo andiphatikize pamodzi ndi anthu olungama).<sup>2</sup>

### Ngale 29 Madani zanzeru za Azaan komanso Iqamat

- ❖ M'ma Swalah onse asanu, azaan komanso iqamat ndi Sunnat kifaya pa Jama'at ndi Sunnat ain kwa amene amaswali popanda jama'at.<sup>3</sup>
- ❖ Ngati azaan komanso iqamat ndi za pajamaat, kukuwa (Jahar) ndiyofunika mmenemo. Choncho nkofunika kuti kalima'at yake yonse inwedwe ndi [munthu] mmodzi, ndipo ngati zili za inu nokha [popemphera Swalah

---

<sup>1</sup> Tohfa al Muhtaj m'a Hashiyah Sharwani, juz. 2, p. 112

<sup>2</sup> Tohfa al Muhtaj, juz. 2, p. 216

<sup>3</sup> Tohfa al Muhtaj m'a Hashiyah Sharwani, juz. 2, p. 78

Ubwino komanso Malamulo apa Azaan (Shafa' i)

popanda jama'at], zikwanira malinga ngati inu mukuzinva nokha.<sup>1</sup>

- ❖ Pamene azaan ayitanidwa kwa anthu a m'deralo, pamafunika kuti achitike munthu [atayima] pamalo okwera uku akukweza mawu kuti amene akunvetsera anvetsetse. Ngati muli ndi cholinga chochita azaan, ndizokwanira kuyitana azaan pakati pa nzikiti komanso mawu okweza kuti munve nokha, ndipo ngati pali cholinga chochita azaan kwa anthu opezeka m'masjid, n'kokwanira kuyitanira azaan pakati pa nzikiti mokweza mawu kuti anthu amene akupezekamo anvetserere.<sup>2</sup>
- ❖ Ndi Sunnah kuwonjezera mawu panthawi ya azaan. Kwa munthu amene akupemphera swalah popanda Jamaat, mawuwo ayenera kukhala amphanvu kuposa mmene anganvere, ndipo pa Jamaat, mawuwo ayenera kunveka mokweza kwambiri kuti anthu oposa mmodzi anve. Sunnah yathunthu ndikuti munthu akweze mawu ake momwe angathere popanda kukumana ndi vuto lililonse. Komabe, ndi Sunnah kuchepetsa mawu pamalo pamene pali nzikiti ndi madrasah pomwe anthu amaswali.<sup>3</sup>
- ❖ Kupatula Fajr azaan, kwa ma azaan a Swalah zonse, ndikofunikira kuti nthawi ya salah ikhale itayamba kale

---

<sup>1</sup> *Ia'nat al-Talibeen*, juz. 1, pp. 400-401

<sup>2</sup> *Fatawa Kubra Fiqhia*, juz. 1, p. 189

<sup>3</sup> *Ia'nat al-Talibeen*, juz. 1, pp. 404-405

kuti azaan achitike. Ngati azaan itayitanidwa nthawi isanayambe, sizingakhale zoloredwa. Komabe, Fajr azaan imatha kuyitanidwa pakati pa usiku. Chifukwa chake, azaan ayenera kuyitanidwa nthawi ikayamba. Ngati itayitanidwa nthawi isanakwane, kapena muezzin wayamba kuyitana azaan nthawi isanakwane komanso nthawi ikuyamba, ayenera kubwereza azaan pazochitika zonse ziwiri.<sup>1</sup>

- ❖ Ma Muezzin ayenera kuwona ndandanda wa nthawi ya salah pafupipafupi. M'malo ena, ma muezzin amayamba azaan nthawi isanayambe. Ma Imamu komanso makomiti a nzikiti akupemphedwa kuti ayiyang'anire bwino nkhanayi.

**Chidziwitso:** Nkoyenera kwa amene asankhidwa kukhala muazin kudziwa nthawi ya Swalah. Ndi haram kumuyika munthu kukhala muazin amene satha kudziwa nthawi ya swalah, ngakhale azaan yake [yomwe amayitanira pa nthawi ya swalah] ili yolondola. Kuwonjezera apo, kuli kofunikiranso kwa iye [muezzin] kukhala wankulu, wanzeru ndi wowona ntima.<sup>2</sup>

- ❖ Pa Swalah ya Fajr, ma Azaan awiri ndi Sunnah: imodzi [pambuyo pakati pa usiku] nthawi ya Fajr isanayambike, ndipo ina poti nthawi ya Fajr itayambika. Ngati

---

<sup>1</sup> *Majmou' Sharh al-Mazhab*, juz. 4, p. 116

<sup>2</sup> *Tohfa-tul-Muhtaj*, juz. 1, pp. 212-213

Ubwino komanso Malamulo apa Azaan (Shafa' i)

mukufuna kukhutitsidwa ndi azaan imodzi yokha, ndibwino kuchita azaan nthawi ya Fajr itayamba.<sup>1</sup>

- ❖ Ndi Sunnat kukhala ndi ma muazin awiri pa nzikiti komanso pa malo aliwonse otere omwe amachitirako Swalah ya Jamaat. Muazin m'modzi ayitane Azaan nthawi ya Fajr isanayambike, ndipo winayo ayitanire Azaan nthawi ya Fajr ikakwana koma Fajir isanapempheredwe.<sup>2</sup>
- ❖ Akazi adzikonzera okha Jamaat kapena kuswali popanda Jamaat, Azaan si Sunnah kwa iwo. Komabe, iqamat ndi Sunnah kwa iwonso.<sup>3</sup>
- ❖ Azaan komanso iqamat zoyitanidwa ndi mkazi sizovomerezeka kwa amuna ndi adindo. Momwemonso, azaan ndi iqamat yoyitanidwa ndi mdindo sizoyenera kwa amuna kapena kwa adindo ena.<sup>4</sup>
- ❖ Azaan yoyitanidwa ndi munthu wamisala, ana opanda nzeru ndi munthu woledzera, sikoyenera [ndiye kuti ngati mmodzi wa iwo ayitana azaan kapena iqamat, idzakhala yosavomerezeka.]<sup>5</sup>
- ❖ Azaan komanso iqamat yoyitanidwa ndi wopyola malire, ana ozindikira, wakhungu [omwe palibe amene angamuwuze nthawi ya Swalah ikayamba], amene ghusl

---

<sup>1</sup> *Al Manhaj al-Qaweem*, p. 166

<sup>2</sup> *Tohfa-tul-Muhtaj*, juz. 1, p. 215

<sup>3</sup> *Tohfa-tul-Muhtaj*, juz. 1, p. 210

<sup>4</sup> *Tohfa-tul-Muhtaj*, juz. 1, p. 213

<sup>5</sup> *Al-Manhaj al-Qaweem*, p. 162

Ubwino komanso Malamulo apa Azaan (Shafa' i)

ili fard kwa iye kapena wopanda wudhu ndi makruh. Komabe, [kusi yana kwake ndikwakuti] ngati wopyola malire, mwana woganiza bwino kapena wakhungu ayitanira azaan, palibe choyipitsidwa m'zimenezi (ngati munthu amene ghusl ili fard kwa iye, kapena wopanda wudhu., adziyitana azaan kwa iye mwini kapena ku Jamaat, sizimakondedwa m'zochitika zonse ziwirizi.)<sup>1</sup>

- ❖ Ndi Sunnat kuti amene ayitana azaan ndi iqamat akhale ndi Mawu okwera komanso abwino; akhale wolungama, mbadwa ya muazin wa wokondedwa Mtumiki صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ<sup>2</sup> ndikugwira ntchito popanda malipiro aliwonse.<sup>3</sup>
- ❖ Ndi Sunnah kuti azaan ichitidwe pafupi ndi nzikiti poyang'ana ku Qiblah ndi kuyika zala zakutsogolo m'makutu. Komabe, sizili Sunnah kuyika zala m'makutu kwa amene akuyitanira azaan yekha ndi mawu otsika.<sup>4</sup>
- ❖ Kwa amene ali wodziwa kuyitanira azaan ndi iqamat ndi kutsogolera Swalah, ndi mustahab kuchita zonsezi.<sup>5</sup>
- ❖ Tarjee ndi Sunnah panthawi ya azaan, kunena kuti أَشْهَدُ أَنْ لَا إِلَهَ إِلَّا اللَّهُ kawiri komanso أَشْهَدُ أَنَّ مُحَمَّدًا رَسُولُ اللَّهِ muntima kawiri asananene mokweza.<sup>6</sup>

---

<sup>1</sup> Bushra al-Kareem, p. 188

<sup>2</sup> Tohfah-tul-Muhtaj, juz. 1, p. 213

<sup>3</sup> Al-Manhaj, al-Qaweem, p. 164

<sup>4</sup> Tohfah-tul-Muhtaj, juz. 1, p. 212

<sup>5</sup> Al-Manhaj, al-Qaweem, p. 168; Nihaya-tul-Muhtaj, juz. 1, p. 261

<sup>6</sup> Tohfah-tul-Muhtaj, juz. 1, p. 211, imechagulia

Ubwino komanso Malamulo apa Azaan (Shafa' i)

- ❖ Ndi Sunnat kutembenezira nkhope yako mbali yakumanja nthawi zonse ziwiri pamene ukunena **حَيَّ عَلَى الصَّلَاةِ** ndi mbali yakumanzere nthawi zonse ziwiri poti **حَيَّ عَلَى الْفَلَاحِ**,<sup>1</sup> ngakhale itakhala azaan ya khutbah kapena ukudziyitanira azaan iwe wekha.<sup>2</sup> Nkhope iyenera kutembenezidwa basi, osati chifuwa.<sup>3</sup> Pali ena muazin amene amasuntha nkhope zawo kumanja ndi kumanzere mokoma pang'ono ponena kuti **الْفَلَاحِ** komanso **الصَّلَاةِ**; ndi njira yolakwika. Njira yolondola ndikutembenezira nkhope moyenera kumanja ndi kumanzere kenako ndikuyamba kunena mawu akuti **حَيَّ عَلَى الْفَلَاحِ**.<sup>4</sup>
- ❖ M'ma Azaan a Fajr ndi Sunnah kunena kuti **الصَّلَاةُ خَيْرٌ مِنَ النَّوْمِ** kawiri pambuyo pa **حَيَّ عَلَى الْفَلَاحِ**.<sup>5</sup>
- ❖ Ndi Sunnat kwa Muazin kunena **‘أَلَا صَلُّوا إِنِّي رَحَالِكُمْ** [kawiri] pambuyo pake. **حَيَّ عَلَى الْفَلَاحِ** pa nthawi ya nvula yamphanvu, mdima wandiweyani ndi mphepo yankuntho yamphanvu, ndipo nzabwino kwambiri kunenedwa pambuyo pa kutha kwa azaan.<sup>6</sup>

---

<sup>1</sup> Tohfah-tul-Muhtaj, juz. 1, p. 212; Al-Manhaj al-Qaweem, p. 164

<sup>2</sup> Ia'nat al-Talibeen, juz. 1, p. 404

<sup>3</sup> Tohfah-tul-Muhtaj, juz. 1, p. 212

<sup>4</sup> Rauzah al-Talibeen, juz. 1, p. 310

<sup>5</sup> Tohfah-tul-Muhtaj, juz. 1, p. 211

<sup>6</sup> Hashiya Sharwani Ala Tohfa al-Muhtaj, juz. 2, p. 112

- ❖ Ndi mustahab kuwerenga Ayat-ul-kursi pakati pa azaan ndi iqamat.<sup>1</sup>
- ❖ Ndi Sunnat kuswali [pakati pa azaan ndi iqamat] popeza Swalaat yoteroyo siyikanidwa.<sup>2</sup>
- ❖ Kupatula Maghrib, kuchedwetsa kunena iqamah pambuyo pochita Azaan mpaka kuti anthu asonkhane [kuti apite ku Jamaat] ndi Sunnah.<sup>3</sup>
- ❖ Ndi mustahab kunena iqamah pamalo ena motalikirana ndi pamalo pomwe anayitanira azaan, ndipo amene wachita azaan achitenso iqamah.<sup>4</sup>
- ❖ Zili Sunnat kunfunira zabwino wokondedwa Mtumiki ﷺ musanayambe azaan komanso iqamah.<sup>5</sup>
- ❖ Nenani ma kalimaat a iqamat mwachangu ndipo nenani makalimaat awiri mu mpweya womwewo.<sup>6</sup>
- ❖ Imirirani kuswali pambuyo pomaliza kunena Qadi qamat swalah. Komabe, ngati wina atenga nthawi yoyimirira ndikumawopa kuti sangathe kupeza ubwino wa takbeer-e-tahreemah pamene wayimirira pambuyo pomaliza

---

<sup>1</sup> *Fath al-Mu'een*, p. 158

<sup>2</sup> *Tohfah-tul-Muhtaj*, juz. 1, p. 217

<sup>3</sup> *Tohfah-tul-Muhtaj*, juz. 1, p. 217

<sup>4</sup> *Al-Manhaj*, al-Qaweem, p. 169

<sup>5</sup> *Fatah al Mu'een*, p. 157

<sup>6</sup> *Tohfah-tul-Muhtaj*, juz. 1, p. 211



Ubwino komanso Malamulo apa Azaan (Shafa' i)

iqamah, ayimirire pa nthawi yomwe ali wotsimikiza kuti adzakhala. wokhoza kupeza ubwino wonena takbeer-e-tahreemah ndi imam.<sup>1</sup>

- ❖ Ngati munthu wayimirira ndipo iqamat yayamba, tsopano sizili Sunnah kwa iye kukhala panso kenako n'ku imirira [iqamat ikatha], popeza kuchita kumeneku kudzamchititsa kusalabadira kuyankha moyenera iqamat.<sup>2</sup>
- ❖ Pamene iqamat yatsala pang'ono kuyamba kapena ikuyamba, ndi makruh tanzihhe kwa amene akufuna kulowa mu jamaat kuti achite nafl salah.<sup>3</sup>
- ❖ Ndi Sunnah kwa amene akuchita azaan komanso iqamat ndi amene akunva azaan ndi iqamat kuti anfunire zabwino Mtumiki wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ  
اَللّٰهُمَّ رَبِّ هَذِهِ الدَّعْوَةِ الثَّمَامَةِ وَالصَّلٰوةِ الْقَائِمَةِ اِيَّتِ مُحَمَّدَانِ الْوَسِيْلَةَ وَالْفَضِيْلَةَ وَابْعَثْهُ  
مَقَامًا مَّحْبُوْدًا الَّذِي وَعَدْتَهُ اِنَّكَ لَا تُخْلِفُ الْوَعْدَ<sup>4</sup>
- ❖ Pambuyo poyankha Maghrib azaan komanso kunfunira zabwino Mtumiki ndi mustahab kunena motere:

اَللّٰهُمَّ هَذَا قَبَالُ نَهَارِكَ وَادْبَارُ لَيْلِكَ وَاصْوَاتُ دُعَاتِكَ فَاعْفِرْ لِي

---

<sup>1</sup> Tohfah-tul-Muhtaj, juz. 1, p. 370

<sup>2</sup> Tohfah-tul-Muhtaj, juz. 1, p. 370

<sup>3</sup> Tohfah-tul-Muhtaj, juz. 1, p. 370

<sup>4</sup> Tohfah-tul-Muhtaj ma' Hashiyah Sharwani, juz. 2, pp. 113-114

## Ngale 12 za Madani zoyankhira Azaan ndi Iqamat

- ❖ Ndi Sunnat kuyankha azaan ndi iqamat, ngakhale kwa amene alibe wudhu kapena ghusl ndiyokakamizika kwa iwo kapena amene ali kumwezi.<sup>1</sup>
- ❖ Yankho la tarje'e lidzaperekedwanso ngakhale silinanveke.<sup>2</sup>
- ❖ Ngakhale kwa amene akunvetsera mbali ina ya azaan, kuli mustahab kuyankha azaan kotheratu.<sup>3</sup>
- ❖ Ngati pali ma muezzin angapo ndipo akuchita azaan imodzi pambuyo pa inzake, wonvetsera amayankha onse. Komabe, kwatsindika kwambiri kuyankha azaan woyamba, ndipo kusamuyankha kudzakhala makrūh. Ngati onse ayitana azaan nthawi imodzi, kuyankha azaan m'modzi ndikokwanira.<sup>4</sup>
- ❖ Ngati munthu akhala chete osayankha azaan panthawiyo koma n'kuyankha atamaliza azaan, Sunnah idzawonedwa kuti yachitidwa pokhapokha nthawi yochulukira sinadutse monga momwe inakhazikitsidwa.<sup>5</sup>
- ❖ Kukhala wotanganidwa kuyankhula pa nthawi ya azaan kumayambitsa infa yoyipa.<sup>6</sup>

---

<sup>1</sup> *Tohfah-tul-Muhtaj m'a Hashiyah Sharwani, juz. 2, pp. 106-108, Summarised*

<sup>2</sup> *Ia'nat al-Talibeen m'a Fath al-Mu'een, juz. 1, p. 409*

<sup>3</sup> *Asna al-Matalib, juz. 1, p. 373*

<sup>4</sup> *Ia'nat al-Talibeen, juz. 1, p. 409*

<sup>5</sup> *Tohfah-tul-Muhtaj, Kitab al-Salaat, juz. 1, p. 216*

<sup>6</sup> *Bushra Kareem, p. 188*

Ubwino komanso Malamulo apa Azaan (Shafa' i)

- ❖ Siyani kuwerenga Qur'an yopatulika, kupemphera ndi kuchita zikr, ndi zina zotero kuti muyankhe azaan.<sup>1</sup>
- ❖ Ndi makruh kuyankha azaan ndi iqamat kwa munthu amene ali pakati pa kuchotsa magari akunsana kapena ali kuchimbudzi kapena amene ali pamalo awunve kapena kunvetsera ulaliki. Ngati nthawi siyinadutse atamaliza, ayankhe, ndipo ngati nthawi yayitali yadutsa monga momwe anakhazikitsira, ndiye kuti si mustahab kwa iye kuyankha.<sup>2</sup>
- ❖ Ngati m'kamwa mwa munthu muli modetsedwa, ndi makruh kuti ayankhe [Azaan ndi iqamat] asanayeretse m'kamwa.<sup>3</sup>
- ❖ Ngati Hanafi wanena kalima'at ya iqamat kawiri, yankho liyenera kuperekedwanso kawiri.<sup>4</sup>
- ❖ Pa Azaan ndi iqamat, ndi bwino kusiya kuyenda; kutolera mbale, galasi, kapena chinthu china chirichonse; kusunga chakudya; kusewera ndi ana aang'ono; kulankhula ndi munthu wina pogwiritsa ntchito chinenero chamanja; ndi zina.
- ❖ Panthawi ya azaan, sibwino kupita kuchimbudzi chifukwa sudzatha kuyankha azaan kumeneko, ndipo mwanjira imeneyi, siwudzapatsidwa mphotho yayikulu. Komabe, ngati

---

<sup>1</sup> *Tohfah-tul-Muhtaj*, juz. 1, p. 216

<sup>2</sup> *Tohfah-tul-Muhtaj m'a Hashiyah Sharwani*, juz. 2, p. 110

<sup>3</sup> *Ia'nat al-Talibeen*, juz. 1, p. 410

<sup>4</sup> *Hashiyah Sharwani, Kitab Al-Salaat*, juz. 2, p. 108

Ubwino komanso Malamulo apa Azaan (Shafa' i)  
wina akufunitsitsa kuchita chimbudzi kapena kukodza  
kapena akuwopa kun'dutsa Jamaat, ayenera kupita  
kuchimbudzi.

## **Nthawi 10 zokondedwa (Mustahab) za kuchita Azaan**

Zili Sunnat kuchita azaan

1. m'makutu mwa munthu wokhumudwa,
2. amene ali ndi khunyu,
3. munthu wokwiya kwambiri
4. wawukali komanso
5. wokwiya msanga.
6. pa nthawi yomenyana kwambiri,
7. Pamene moto ukuyaka,
8. Pamene ziwanda zamukhudza; pomwe zili Sunnah kuchita azaan ndi iqamat zonse
9. m'khutu la mwana wobadwa kumene ndi
10. munthu akanyamuka ulendo.<sup>1</sup>

---

<sup>1</sup> *Tohfah-tul-Muhtaj*, vol. 1, p. 209

Ubwino komanso Malamulo apa Azaan (Shafa' i)

## Mfunireni zabwino Mtumiki Wodalitsika

### musanayambe kuchita Azaan

Musanapange azaan komanso iqamat, werengani ‘بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَنِ الرَّحِيمِ’ kenako mizere inayi yotsatira ya swalah ndi salam zodalitsika.

|                                                  |                                  |
|--------------------------------------------------|----------------------------------|
| وَعَلَىٰ آلِكَ وَأَصْحَابِكَ يَا حَبِيبُ اللَّهِ | الصلوة والسلام عليك يا رسول الله |
| وَعَلَىٰ آلِكَ وَأَصْحَابِكَ يَا كَوْنُ اللَّهِ  | الصلوة والسلام عليك يا نبي الله  |

### Kunong'ona kwa Satana

Poti kumfunira zabwino Mtumiki wokondedwa sizinachitikepo kumayambiriro kwa Azaan pamaso pa Mtumiki wokondedwa صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ mu nthawi ya moyo wake ngakhale muwulamuliro wa ma Khalifa anayi odalitsika, kuchita zimenezi ndi kusokonekera ndi kusokera. (مَعَادُ اللَّهِ)

### Yankhani kunong'oneza kwa satana uku

Ngati mfundo imeneyi ivomerezedwa kuti kuchita chilichonse chotere chimene sichinachitike m'nthawi yodalitsika imeneyo ndi nzeru zatsopano ndiponso ndi uchimo, dongosolo lonse limene lilipo lidzasokonezedwa. Zitsanzo 12 zokha mwa zitsanzo zosawerengeka zikuperekedwa pofuna kunvesetsa bwino lomwe kuti zimenezi sizinachitike m'nthawiyo, komabe zikuchitidwa ndi aliyense m'nthawi ino.

1. Hajjaj Bin Yusuf anayambitsa madontho ndi zizindikiro

Ubwino komanso Malamulo apa Azaan (Shafa' i)  
mu Qur'an yopatulika m'chaka cha 95 AH.

2. Anayambanso kugwiritsa ntchito zilembo zoyima kumapeto kwa vesi lililonse.
3. Kusindikizidwa kwa Qur'an yopatulika mu mawonekedwe ammapepala ngati B uku.
4. M'mbuyomu, pakatikati pa nzikiti panalibe khoma loti imamu ayime. M'nthawi ya Ulamuliro wa Walid Marwani, Sayyiduna Umar bin Abdul 'Aziz رَحِمَیَ اللہُ عَنْہُ anayiyambitsa, yomwe tsopano ikupezeka mu msikiti uliwonse.
5. makalimaat asanu ndi limodzi.
6. Kudziwa za Sarf ndi Nahw.
7. Kudziwa za Hadees ndi mitundu yake [yosiyanasiyana].
8. Dars-e-Nizami.
9. Malamulo anayi a Shari'at komanso tareeqat.
10. Kulankhula mawu a Cholinga mu salah.
11. Ulendo wa Haji pa ndege.
12. Jihad yokhala ndi zida zasayansi zasopano.

M'nthawi yathu ino palibe amene amawona chilichonse mwa zochita zomwe tatchulazi kuti ndi tchimo ngakhale kuti zinalibe m'nthawi yodalitsika, nanga n'chifukwa chani kungomfunira zabwino Mtumiki wokondedwa صَلَّى اللہُ عَلَیْہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم

Ubwino komanso Malamulo apa Azaan (Shafa' i)

pa Azaan komanso Iqamat amaziwona ngati tchimo! Kumbukirani, kusakhalapo kwa umboni wa kusalolezedwa kwa chinthu chilichonse ndi umboni wa kuloledwa kwake. Mosakayikira, mchitidwe uliwonse watsopano wotere womwe Shari'ah siwunaletse, ndikusintha kwabwino komanso kovomerezeka, ndipo ndi mfundo yosatsutsika kuti kumfunira Mtumiki zabwino Azaan asanayambe sikunaletsedwe mu Hadith iliyonse. Chifukwa chake, kusapezeka kuletsedwa kumabweretsa chilolezo. Wokondedwa Mtumiki ﷺ mwiniwake anawonetsa kukopa pakuyambitsa zinthu zabwino mu Chisilamu. Choncho Hadith yomwe yatchulidwa m'ndime ya 'Kitab-ul-'Ilm ya Sahih Muslim ikuti:

مَنْ سَنَّ فِي الْإِسْلَامِ سُنَّةً حَسَنَةً فَعَمِلَ بِهَا بَعْدَهُ كُتِبَ لَهُ مِثْلُ أَجْرِ مَنْ عَمِلَ بِهَا وَلَا يَنْقُصُ مِنْ أَجُورِهِمْ شَيْءٌ<sup>1</sup>

'Amene adzayambe njira iliyonse yabwino mwa Asilamu, kenako nkutsatiridwa pambuyo pake, malipiro a otsatira adzalembedwanso m'buku la ntchito za amene anayiambitsa, ndipo malipiro a otsatira ake sadzachepetsedwa.

Mwa kuyankhula kwina, amene wayambitsa chabwino chilichonse mu Chisilamu akuyenera kulandira malipiro aakulu. Momwemonso, mopanda chikayiko, munthu wamwayi yemwe wayamba chizolowezi chomfunira zabwino kwa wokondedwa Mtumiki ﷺ asanayambe azaan

---

<sup>1</sup> Muslim, p. 1031, Hadith 1017

komanso iqamat nayenso akuyenera kulandira malipiro osatha. Iye pamodzi ndi Asilamu amene akuchita zimenezo mpaka tsiku lachiweruzo adzapeza malipiro popanda kuchepetsedwa malipiro a aliyense.

Apa, pakhoza kubwera funso m'maganizo mwa munthu woti Hadith yodalitsika ikutanthawuza chani: **كُلُّ بِدْعَةٍ ضَلَالَةٌ وَكُلُّ ضَلَالَةٍ فِي النَّارِ** [Kupeka kulikonse ndi kusokera, ndipo kusokera kulikonse nkwa ku moto].<sup>1</sup> Kodi Hadith yodalitsikayi ikutanthawuza chani? Zikutanthawuza kuti Hadith yodalitsika yomwe tatchulayi ndi yowona. Kunena zowona, liwu loti 'bid'at' lomwe latchulidwa mu Hadith likunena za bid'at sayyi'ah (zatsopano zosokeretsa), ndipo ndithudi bid'at iliyonse yotsutsana kapena yochotsa Sunnat ndi zinthu zatsopano zosokeretsa. Choncho Sayyiduna Shaykh 'Abdul Haq Muhaddis Dehlvi wanena kuti Bid'at iliyonse yomwe ikugwirizana ndi mfundo za Sunnah ndipo yosasemphana ndi Shari'ah ndi Sunnah ndi bid'at hasanah. Bid'ah yomwe ili yotsutsana ndi Shari'ah komanso Sunnah ndi bid'at yosochera, kutanthawuza "zopeka zosokera."<sup>2</sup>

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللَّهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

Kuti muteteze chikhulupiro chanu, werengani mutu wa 'Mafunso ndi Mayankho okhudza Kufriya Kalimat', kuchokera patsamba 359 mpaka 362 m'buku lamasamba 692, lofalitsidwa

<sup>1</sup> Ibn-e-Khuzaimah, p. 414, Hadithi 1785

<sup>2</sup> Ashat al-Lama'at, juz. 1, p. 125



Ubwino komanso Malamulo apa Azaan (Shafa' i)

ndi Maktaba-tul-Madina, Nthambi yosindikiza mabuku ya Dawat-e-Islami:

## Mafunso ndi mayankho okhuza kusalemekeza Azaan

**Funso:** Mukuti bwanji za kusalemekeza azaan?

**Yankho:** Azaan ndi chimodzi mwa zizindikiro za Chisilamu. Kusalemekeza chizindikiro chilichonse cha Chisilamu ndiko kufr (kusakhulupirira).

## Kuchita nthabwala ndi mawu woti حَيَّ عَلَى الصَّلَاةِ

Funso: Mukutanthawuza chani ponena kuti, 'Bwerani kunyumba ya kanema, apo ayi matikiti atha!' mu nthabwala panthawi ya azaan pambuyo ponva حَيَّ عَلَى الصَّلَاةِ ("mwachitsanzo" bwerani ku Swalah) kapena حَيَّ عَلَى الْقَلَامِ ("mwachitsanzo" bwerani ku chipulumutso)?

Yankho: Ndi kufr, chifukwa مَعَآذَ اللَّهِ kuli ngati kuseka azaan. Imam Ahmad Raza Khan رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ anafunsidwa funso, "Mukuti chani pa izi? Zaid wachitira chipongwe azaan yemwe anayitanidwa ndi muezzin wa pa msikiti, mwachitsanzo atanva chiganizo حَيَّ عَلَى الصَّلَاةِ, anachita chipongwe motere: [Bhaya lath challa.] Adzakhala wosakhulupirira nthawi yomweyo komanso nikah yake idzawonongeka. Chitsanzo chagwiritsidwa ntchito kwa Zaid kapena ayi, ndipo Nikah yake yasanduka yopanda pake kapena ayi?"

Ubwino komanso Malamulo apa Azaan (Shafa' i)

Yankho: Ndithu, ndi kufr kumpangira nthabwala azaan. Ngati wachitadi kuseka azaan, ndithudi, wasanduka kafiri, ndipo nikah yake ndi nkazi wake yasanduka yopanda pake. Ngati alowa m'Chisilamu ayenera kuchitanso nikah ndi nkazi wake, ndiye kuti kuchita banja kudzakhala halal, apo ayi kudzakhala kuti akuchita chiwerewere nthawi zonse. Kuwonjezera apo, ngati nkaziyo atavomera kuchita naye zachikondi popanda kuchitanso shahada kulowa Chisilam ndikuchitanso nikah, adzakhalsanso wochita chiwerewere. Koma ngati analibe chitsimikizo chochitira chipongwe Azaan, koma wachitira chipongwe muazin chifukwa Muazin akunena [chiganizochochi] molakwika, choncho pankhaniyi [iye sadzakhala kafiri, ndiponso nikah yake siyidzakhala yopanda pake., koma] iye [Zaid] adzalamulidwa kukonzanso Chisilamu chake ndi nikah.

<sup>1</sup>والله اعلم

## Zitsanzo zisanu ndi zitatu za ziganizo za Kufriyah zokhudza Azaan

1. Munthu amene amaseka azaan ndi wosakhulupirira.<sup>2</sup>
2. Kunyoza kwa azaan kuti, 'Kulira kwa belu kuli bwino kwambiri podziwitsa anthu za salah' ndiko kusakhulupirira.

---

<sup>1</sup> Fatawa Razawiyyah, juz. 21, p. 215

<sup>2</sup> Kufriyah Kalimat kay baray mayn Suwal Jawab, p. 361

Ubwino komanso Malamulo apa Azaan (Shafa' i)

3. Ngati wina anena kwa amene akuchita Azaan kuti, 'Wanama,' adzakhala wosakhulupirira.<sup>1</sup>
4. Ngati wina akunena zotsatirazi za muezzin pamene akuseka azaan kuti, 'Kodi munthu wolandidwa ameneyu akufuwula chani?' kapena kunena za azaan kuti, 'Ndi liwu losatchuka', kapena kuti, 'Ndi mawu a chilendo', choncho zonsezi ndi kusakhulupirira, mwachitsanzo ngati akunena zonsezi monyoza.<sup>2</sup>
5. Ngati wina wachita azaan, kenako wina n'kubwereza azaan pofuna kungosangalala, chigamulo chokhudza kusakhulupirira chidzagwira ntchito kwa munthu wachiwiriyo.<sup>3</sup>
6. Atanva azaan, wina akanena kuti, ' *N'chifukwa chani mukuphokosera!*' ndi ukafiri malinga ngati munthuyo anena chiganizo ichi chifukwa chakuti sakonda azaan.<sup>4</sup>

## Azan

|                                              |                                              |
|----------------------------------------------|----------------------------------------------|
| اَللّٰهُ اَكْبَرُ اَللّٰهُ اَكْبَرُ          | اَللّٰهُ اَكْبَرُ اَللّٰهُ اَكْبَرُ          |
| Mulungu ndi wankulu;<br>Mulungu ndi wankulu. | Mulungu ndi wankulu;<br>Mulungu ndi wankulu. |

---

<sup>1</sup> Fatawa Qazi Khan, juz. 3, p. 513

<sup>2</sup> Minah al-Raud, al Azhar, p. 495

<sup>3</sup> Mujm'a al-Anhar, juz. 2, p. 509

<sup>4</sup> Aalamgiri, juz. 2, p. 290

|                                                                        |                                                                        |
|------------------------------------------------------------------------|------------------------------------------------------------------------|
| أَشْهَدُ أَنْ لَا إِلَهَ إِلَّا اللَّهُ ط                              | أَشْهَدُ أَنْ لَا إِلَهَ إِلَّا اللَّهُ ط                              |
| Ndikuchitira umboni kuti palibe wopembedzedwa mwachowonadi koma Allah. | Ndikuchitira umboni kuti palibe wopembedzedwa mwachowonadi koma Allah. |
| أَشْهَدُ أَنَّ مُحَمَّدًا رَسُولُ اللَّهِ ط                            |                                                                        |
| Ndikuchitira umboni kuti Muhammad ﷺ ndi Mtumiki wa Allah.              |                                                                        |
| أَشْهَدُ أَنَّ مُحَمَّدًا رَسُولُ اللَّهِ ط                            |                                                                        |
| Ndikuchitira umboni kuti Muhammad ﷺ ndi Mtumiki wa Allah.              |                                                                        |
| حَيَّ عَلَى الصَّلَاةِ ط                                               | حَيَّ عَلَى الصَّلَاةِ ط                                               |
| Bwerani ku mapemphero. (Salah)                                         | Bwerani kumapemphero. (Salah)                                          |
| حَيَّ عَلَى الْفَلَاحِ ط                                               | حَيَّ عَلَى الْفَلَاحِ ط                                               |
| Bwerani ku chipulumutso.                                               | Bwerani ku chipulumutso.                                               |
| اللَّهُ أَكْبَرُ اللَّهُ أَكْبَرُ ط                                    |                                                                        |
| Mulungu ndi wankulu; Mulungu ndi wankulu.                              |                                                                        |
| لَا إِلَهَ إِلَّا اللَّهُ ط                                            |                                                                        |
| Palibe wopembedzedwa mwachowonadi koma Allah.                          |                                                                        |

Ubwino komanso Malamulo apa Azaan (Shafa' i)

## Iqamat

|                                                                                                 |                         |
|-------------------------------------------------------------------------------------------------|-------------------------|
| الله أكبر الله أكبر                                                                             |                         |
| Allah ndi wankulu; Allah ndi wakulu.                                                            |                         |
| أَشْهَدُ أَنْ لَا إِلَهَ إِلَّا اللَّهُ                                                         |                         |
| Ndikuchitira umboni kuti palibe wopembedzedwa mwachowonadi koma Allah.                          |                         |
| أَشْهَدُ أَنْ مُحَمَّدًا رَّسُولُ اللَّهِ                                                       |                         |
| Ndikuchitira umboni kuti Muhammad صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ ndi Mtumiki wa Allah. |                         |
| حَيَّ عَلَى الصَّلَاةِ                                                                          |                         |
| Bwerani kumapemphero (salah)                                                                    |                         |
| حَيَّ عَلَى الْفَلَاحِ                                                                          |                         |
| Bwerani ku chipulumutso.                                                                        |                         |
| قَدْ قَامَتِ الصَّلَاةُ                                                                         | قَدْ قَامَتِ الصَّلَاةُ |
| Pemphero layamba.                                                                               | Pemphero layamba.       |
| الله أكبر الله أكبر                                                                             |                         |
| Mulungu ndi wankulu; Allah ndi wankulu.                                                         |                         |
| لَا إِلَهَ إِلَّا اللَّهُ                                                                       |                         |
| Palibe wopembedzedwa mwachowonadi koma Allah.                                                   |                         |

Ubwino komanso Malamulo apa Azaan (Shafa' i)

## Pemphero (Du'a) potha kuchita azaan komanso iqamat

Pambuyo pa Azaan, Muadhini, muqem (omwe akunena iqamat) komanso onvera amfunire zabwino Mtumiki wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ kenako ndichita pempho (Du'a) ili:

اللَّهُمَّ رَبِّ هَذِهِ الدَّعْوَةِ الشَّامَةِ، وَالصَّلَاةِ الْقَائِمَةِ، آتِ مُحَمَّدًا الْوَسِيلَةَ

O Allah! Mfumu ya dawat tammah komanso pemphero (salah) lokhazikitsidwa ili! Perekani kwa bwana wathu, Sayyiduna Muhammad صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ, unkhala pakati

وَالْفَضِيلَةَ، وَابْعَثْهُ مَقَامًا مَحْبُودًا الَّذِي وَعَدْتَهُ،

Ndipo fadilah(kupambana) ndi mawudindo apamwamba, ndipo muyimitseni pa Maqam Mahmud amene munamulonjeza.

إِنَّكَ لَا تُخْلِفُ الْبِعَادَ

Ndithu, Inu simuchita chilichonse chotsutsana ndi Lonjezo Lanu.

## Uthenga wabwino wopembedzera

Wokondedwa Mtumiki صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ wati: “Mukanvera azaan, nenani mawu amene Muadhini wanena, kenako

Ubwino komanso Malamulo apa Azaan (Shafa' i)

ndifunireni zabwino, mukatero mpemphani chiwombolo chifukwa chiwombolo changa chidzakhala chokakamizika kwa amene amapempha zachiwombolo changa.”<sup>1</sup>

### Iman Mufassal [Chikhulupiro mwatsatanetsatane]

|                                                                                                                                                    |
|----------------------------------------------------------------------------------------------------------------------------------------------------|
| أَمَنْتُ بِاللَّهِ وَمَلَكَيْتِهِ وَكُتُبِهِ وَرُسُلِهِ وَالْيَوْمِ الْآخِرِ                                                                       |
| Ndikukhulupirira mwa Allah, Angelo Ake, mabuku Ake (ovumbulutsidwa), Aneneri ake ndi tsiku lachiweruzo.                                            |
| وَالْقَدْرَ خَيْرًا وَشَرًّا مِنَ اللَّهِ تَعَالَى وَالْبَعْثَ بَعْدَ الْمَوْتِ ط                                                                  |
| Ndipo (ndikukhulupirira kuti) mathero abwino kapena oyipa amachokera kwa Mulungu, ndipo (ndikukhulupirira kuti) Kudzakhala kuwuka pambuyo pa infa. |

### Iman Mujmal [Chikhulupiro Mwachidule]

|                                                                                                                      |
|----------------------------------------------------------------------------------------------------------------------|
| أَمَنْتُ بِاللَّهِ كَمَا هُوَ بِأَسْمَائِهِ وَصِفَاتِهِ وَقَبِلْتُ جَمِيعَ أَحْكَامِهِ                               |
| Ndikukhulupirira mwa Allah monga Iye ali ndi mayina Ake onse ndi makhalidwe Ake, ndipo ndavomereza malamulo Ake onse |

---

<sup>1</sup> Muslim Kitab al-Salaat, p. 151, Hadith 384, summarized

اقْرَأْ مِرَاللِّسَانِ وَتَصْدِيقُ مِرَالْقَلْبِ ط

povomereza ndi lilime langa ndikuwachitira umboni ndi  
ntima wanga.

### Kalimah Tayyib (kutanthawuza mawu oyera)

لَا إِلَهَ إِلَّا اللَّهُ مُحَمَّدٌ رَّسُولُ اللَّهِ ط

Palibe wopembedzedwa mwachowonadi koma Mulungu;  
Muhammad صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ ndi Mtumiki wa Allah.

### Kalimah yachiwiri Shahadah (kutanthawuza kuchitira umboni)

أَشْهَدُ أَنْ لَا إِلَهَ إِلَّا اللَّهُ وَحْدَهُ لَا شَرِيكَ لَهُ وَأَشْهَدُ

Ndikuchitira umboni kuti palibe wopembedzedwa  
mwachowonadi koma Allah. Iye ali yekha, ndipo alibe  
wothandizana naye, ndipo ndikuchitira umboni

أَنَّ مُحَمَّدًا عَبْدُهُ وَرَسُولُهُ ط

kuti ndithu, Muhammad صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ ndi kapolo Wake  
ndi Mtumiki Wake.



Ubwino komanso Malamulo apa Azaan (Shafa' i)

### Kalimah Tamjeed (kutanthawuza ukulu)

سُبْحَنَ اللَّهِ وَالْحَمْدُ لِلَّهِ وَلَا إِلَهَ إِلَّا اللَّهُ وَاللَّهُ أَكْبَرُ ط

Ulemerero ukhale wa Allah Wamphanvu zonse, ndipo kuyamikidwa konse nkwa Allah Wamphanvu zonse, komanso palibe wopembedzedwa mwachowonadi koma Allah, ndipo Allah ndi wankulu;

وَلَا حَوْلَ وَلَا قُوَّةَ إِلَّا بِاللَّهِ الْعَلِيِّ الْعَظِيمِ ط

ndipo mphanvu zodzitetezera kumachimo ndi tawfeeq komanso kuchita zabwino zonse zimachokera kwa Allah, Yemwe ndi wankulu.

### Kalimah Tawhiyd Yachinayi (kutanthauza umodzi)

لَا إِلَهَ إِلَّا اللَّهُ وَحْدَهُ لَا شَرِيكَ لَهُ ط لَهُ الْمُلْكُ وَلَهُ الْحَمْدُ

Palibe wopembedzedwa mwachowonadi koma Allah. Ali yekha. Alibe mnzake. Ufumu wonse ngwa Iye, ndipo kutamandidwa konse nkwa Iye.

يُحْيِي وَيُمِيتُ وَهُوَ حَيٌّ لَا يَمُوتُ أَبَدًا ط ذُو الْجَلَالِ وَالْإِكْرَامِ ط

Amapereka moyo, ndipo amapereka infa. Iye ali wamoyo; infa sidzafika kwa Iye; wankulu komanso wolemekezeka.

بِيَدِهِ الْخَيْرُ وَهُوَ عَلَى كُلِّ شَيْءٍ قَدِيرٌ

M'dzanja Lake muli ubwino, ndipo lye Ngokhoza  
chilichonse.

### Chachisanu Kalimah Istighfar (kutanthawuza kufunafuna chikhululuko)

أَسْتَغْفِرُ اللَّهَ رَبِّي مِنْ كُلِّ ذَنْبٍ أَذْنَبْتُهُ عَبْدًا أَوْ خَطَايِمًا

Ndikupempha chikhululuko kwa Allah Yemwe ndi Mbuye  
wanga chifukwa cha machimo onse amene ndachita  
modziwa kapena mosadziwa.

أَوْ عَلَانِيَةً وَأَتُوبُ إِلَيْهِ مِنَ الذَّنْبِ الَّذِي أَعْلَمُ وَمِنَ الذَّنْبِ

kapena mowonekera, ndikulapa machimo amene  
ndikuwadziwa ndi machimo amene sindikuwadziwa.

الَّذِي لَا أَعْلَمُ إِنَّكَ أَنْتَ عَلَّامُ الْغُيُوبِ وَسَتَّارُ الْغُيُوبِ وَعَقَّارُ الذُّنُوبِ

(E, Allah!) Ndithu, Inu Ndinu Wodziwa ghuyub (zobisika)  
ndi Wobisa machimo onse, Wokhululukira machimo onse.

Ubwino komanso Malamulo apa Azaan (Shafa' i)

وَلَا حَوْلَ وَلَا قُوَّةَ إِلَّا بِاللَّهِ الْعَلِيِّ الْعَظِيمِ

ndipo mphanvu zodzitetezera kumachimo ndi mphanvu  
zochitira zabwino zimachokera kwa Allah Yemwe ndi  
wankulu.

### Kalimah Yachisanu ndi chimodzi Radd Kufr (kutanthawuza kukana kusakhulupirira)

اَللّٰهُمَّ اِنِّیْ اَعُوْذُ بِكَ مِنْ اَنْ اُشْرِكَ بِكَ شَيْئًا وَاَنَا اَعْلَمُ بِهٖ

E, Allah, ine ndikudzitchinjiriza kwa Inu kuti ndisaphatikize  
Inu ndi chilichonse ndikudziwa.

وَاَسْتَغْفِرُكَ لِمَا لَا اَعْلَمُ بِهٖ تُبْتُ عَنْهُ وَتَبَرَّأْتُ

Ndipo ine ndikupempha chikhululuko Kwa Inu chifukwa  
cha (Shirk) imene sindiyidziwa. Ndikulapa ndipo  
ndikunyansidwa ndi Kusakhulupirira, kupembedza mafano;

مِّنَ الْكُفْرِ وَالشِّرْكِ وَالْكَذِبِ وَالْغِيبَةِ وَالْبِدْعَةِ وَالنَّبِيِّتِ وَالْفَوَاحِشِ

zabodza, miseche, (zoipa) zatsopano, kukamba nthano,  
zamanyazi,

وَالْبَهْتَانِ وَالْبَعَايِ كُلِّهَا وَأَسْلَمْتُ وَأَقُولُ لَا إِلَهَ إِلَّا اللَّهُ مُحَمَّدٌ رَّسُولُ اللَّهِ ط

zoneneza ndi machimo onse. Ndalowa Chisilamu ndikunena kuti palibe wopembedzedwa mwachowonadi koma Allah, Muhammad ﷺ ndi Mtumiki wa Allah.

### Perekani kabukuka kwa wina mukawerenga nokha

Gawirani timabuku ndi timapepala tokhala ndi ngale zanzeru za Madani zofalitsidwa ndi Maktaba-tul-Madinah pa nthawi zawukwati, nthawi zachisoni, ma 'urs komanso pa Milad, misonkhano yachisilamu ndi nthawi zina kuti mupeze malipiro. Khalani ndi chizolowezi chosunga timabuku mu shopu yanu kuti mupatse makasitomala kwa wulere. Perekani kabukhu kapena kabuku kolimbikitsa Sunnah kamodzi kokhala ndi ngale zanzeru za Madani kwa munthu amene akupereka nyuzipepala kapena kwa ana ndipo agawireni mdera lanu kamodzi pamwezi ndipo potero afalitse kuyitanira ku chilungamo.

## Chiwerengero cha ma Muezzin (opereka Adhana) a Mtumiki wa Allah

Mtsogoleri wa ku Madina, Mtumiki wa Allah anali ndi ma Muezzin anayi: (1) Hazrat Bilal (Habshi) bin Rabah رَضِيَ اللّٰهُ عَنْهُ (2) Hazrat Amr ibn Umm Maktum رَضِيَ اللّٰهُ عَنْهُ, onse awiriwa ankapereka Adhana ku Madina Al-Munawwarah. (3) Hazrat Sa'd bin 'Aidh رَضِيَ اللّٰهُ عَنْهُ ku Quba Sharif. (4) ndi Hazrat Abu Mahdhurah رَضِيَ اللّٰهُ عَنْهُ ankapereka Adhana ku Makkah Al-Mukarramah. (Al-Mawahib-ul-Laduniyyah, 1/455)



Faizan-e-Madina, Muhalla Saudagaran, Purani Sabzi Mandi, Karachi

UAN +92 21 111 25 26 92 0313-1139278

www.maktabatulmadinah.com / www.dawateislami.net

feedback@maktabatulmadinah.com / ilmia@dawateislami.net